TICHITENJI MTSIKANA WOLIMBA MTIMA

Wolemba : Whyghtone Kamthunzi

TICHITENJI MTSIKANA WOLIMBA MTIMA

Wolemba : Whyghtone Kamthunzi
Wojambula : Brian Hara

Lilongwe
National Library Service
1996

9

Published by
The Book Development Department
National Library Service
P.O. Box 30314
Lilongwe 3

© National Library Service 1996

First Published 1996

The National Library Service wishes to express gratitude to the Canadian Organisation for Development through Education (CODE) for funding the publication of this book.

All rights reserved. No part of this publication may be copied or transmitted in any form or by any means without permission of the copyright holders.

ISBN: 99908-35-08-X

ZA M'KATIMU

Tsamba

Mutu 1	Tichitenji amusankha kupita ku sekondale	1
Mutu 2	Tichitenji ku sekondale	6
Mutu 3	Tichitenji panjira ya kumudzi	10
Mutu 4	Tichitenji abwerera kusukulu	15
Mutu 5	Tichitenji afika m'tauni	18
Mutu 6	Tichitenji akumana ndi Gwaza kuchipatala	21
Mutu 7	Tichitenji amupima m'chipatala	24
Mutu 8	Tichitenji amva zotsatira za kupima	28
Mutu 9	Tichitenji abwereranso kusukulu	30
	Mafunso	

MUTU 1

TICHITENJI AMUSANKHA KUPITA KU SEKONDALE

Tichitenji anali osangalala kwambiri atamva kuti anamusankha kuti apite ku sekondale. Pasukulu ya m'mudzi mwawo mwa Mfumu Chapita, iye yekha ndiye adamusankha kupita kusekondale. Izi zinali zonyaditsa kwambiri. M'kalasi mwawo munali ana asukulu ambiri koma ochuluka anali anyamata. Zoti iye wapambana yekha pasukulupo, inali nkhani yomwe inali pakamwa pa aliyense. Dzina la Tichitenji linali ponseponse.

"Paja akulu adati chimanga chimalola opanda manu", anthu ena ankanena monyodola akamakamba za mwayi adaupeza Tichitenjiwu. Mawu awa sanali kungowanena chabe koma anali owona kwambiri. Tichitenji anali m'mphawi kwambiri. Bambo a Tichitenji, a Masawo, kokhala kwawo kunali kumowa basi ndipo zosamalira pakhomo analibe nazo ntchito. Iwo zovala zawo zinali nsanza zokhazokha. Ndalama zomwera mowa ankachita kuzipeza m'njira ya maganyu. Iwowa ankakonda kumangoti zungulizunguli kunyumba za aphunzitsi ku sukulu kuti aziwapatsa maganyu. Kunyumba za aphunzitsiku, maganyu omwe ankapezeka mosavuta ndi owaza nkhuni.

Tichitenji naye ngakhale anali okondwera nkusankhidwako, anali ndi nkhawa poganizira kuti mwina mwake akhoza kulephera kupita ku sekondaleko chifukwa chosowa ndalama. Mayi a Tichitenji, a Nanyoni, anali kupita uku ndi uku kunka nafufuza ndalama. Iwo sanafune kuti mwanjira ili yonse mwana wawoyo alephere kupita ku sukulu.

Mayiyo anagulitsa kamtedza komwe anali nako. Komanso popeza anali ndi luso lowumba miphika, analimbikira lusolo. Iwo sankapezeka pakhomo akungokhala ayi.

"Mungozisiya izi, mungozunzika nazo; lathuli sibanja loti nkuphunzitsa mwana ayi. Alipo mabanja odalitsika omwe angathe kuchita zimenezo", a Masawo anali kuuza akazi awo ncholinga chofuna kuwagwetsa mphwayi mayiwo. Koma mayi a Tichitenji sanamvere zimenezi.

"Muwona tizitha bambo, ndipo anthu omwe akutisekawa achita manyazi. Chomwe ndifuna ine nchakuti Tichitenji adzakhale pantchito yapamwamba mtsogolo. Zitadzatero ndiye kuti mitima ya anthu akutisekawa idzaphulika ndi manyazi", a Nanyoni adauza mwamuna wawo.

"Maloto amenewo" a Masawo adatero akutuluka m'nyumba ulendo wakumowa. Uwutu unali m'mawa watsiku lina. Koma a Nanyoni sanagwe mphwayi. Analimbikira pakhama lawo lofunira Tichitenji ndalama zokalipira ku sekondale.

Tichitenji maloto ake anali odzakhala mtolankhani atadzamaliza sukulu. Iye anali asanamuonepo mtolankhani. Iye chidwi chake pa ntchito ya utolankhani chinamudzera tsiku lina akumvera wailesi kunyumba kwa amalume ake. Tsikuli ndi lomwe pulezidenti wa dziko lino ankachokera ku ulendo wocheza ku dziko lina lake. Pulezidentiyo atatsika ndege, anakalowa m'nyumba yolandirira alendo olemekezeka. M'nyumba mmenemu Pulezidentiyo adapeza atolankhani awayilesi komanso amanyuzipepala.

Atolankhani aja anayamba kumufunsa Pulezidenti uja za ulendo wakewo. Mmodzi wa atolankhaniwo anali wa mkazi ndipo anali kufunsa mafunso akupsa zedi. Choncho Tichitenji anachita chidwi ndi momwe mtolankhani wa mkaziyo ankafunsira mafunso pulezidentiyo. Akanakhala kuti pulezidentiyo anali munthu wamba panzeru, bwenzi akulephera kuyankha momveka bwino mafunso ankafunsa mtsikanawo.

Tichitenji sanali kubisa maganizo akewa moti anzake kusukulu ankangomutcha mtolankhani, ndipo mwini wakeyo ankanyadira. Iye anawauzanso aphunzitsi ake



Tichitenji afunsa funso kwa aphunzitsi m'kalasi.

zachikhumbokhumbo chake chodzagwira ntchito ya utolankhaniyo. Aphunzitsi adamulimbikitsa kwambiri. Iwo adati atolankhani achikazi ndiwo anali kunyanya